


Yolembedwa ndi Edward Hughes
Yojambulidwa ndi Byron Unger; Lazarus

Yotathauzidwa ndi Phiri Williams
Yotengedwa ndi M. Maillot; Tammy S.

Nthano 2 ya zili 60

**M1914.org**

**Bible for Children, PO Box 3, Winnipeg MB  R3C 2G1  Canada**

Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.






















Chiyambi chakukwiya kwa munthu

Nthano yochokera mu mau a Mulungu, Baibulo,

opezeka mu

Genesis 3-6

"Polowela pa mau anu pamapasa kuwala."
Masalimo 119:130

**Mulungu adziwa** kuti timachita zinthu zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango chauchimo ndi infa.

**Mulungu amatikonda** kwambiri kotero anatuma mwana wake, Yesu, kutifera pamtanda ndi kulipila chilango. **Yesu anadza wamoyo** ndipo anabwereranso kumwamba wamoyo! Ndipo Mulungu angathe kutikhululukira machimo.

**Ngati mufuna kulapa machimo anu**, nenani izi kwa Mulungu: Mulungu wanga wokondedwa, ndikhulupilira Yesu anandifera ndipo alinso ndi moyo. Chonde lowani mumoyo wanga ndi kundi khululukira ma chimo anga, kuti ndikhale ndi moyo wosatha tsopano, ndipo mukhale ndi ine kwa nthawi zonse. Ndithandizeni kuti ndikhale mwa inu ngati mwana wanu. Amen. Yohane 3:16

**Werenga Baibulo ndikuyankhula ndi Mulungu matsiku onse!**

Chichewa


"Kodi Mulungu anakuuzani kuti musadye mtengo uliwonse?" njoka inafunsa Eva. "Tingathe kudya zipatso zonse koma zamtengowu ayi," Eva anayankha. "Ngati tizadya kapena kugwira zipatso zake, ifeyo tizafa." "Ayi simuzafa." Njoka inanena.
3
"Inuyo muzakhala ngati Mulungu." Ndipo Eva anafuna chipatso chamtengowo. Anamvera njokayo ndipo anadya chipatsocho.
4
Ndipo pamene Eva anachita kusamvera kwa Mulungu anamtsogolera Adamu kuti adye chipatso. Ndipo Adamu anakanena kuti, "ayi! Sindikufuna kusamvera mau a Mulungu."
5
Pamene Adamu ndi Eva atachimwa, ndipo wonse anazindikira kuti alimaliseche.
6
Iwo anazipangira masamba amkuyu. Anadziveka wokha, ndi kukabisala kuthengo kuchoka pamaso pa Mulungu.
7
Kumadzulo Mulungu anabwera kuzayendera kumunda. Iye anadziwa chimene Adamu ndi Eva anachita. Ndipo Adamu anamuda mkazi wake Eva. Ndipo Eva anayida njoka. Mulungu anati, "njoka ndiyotembereredwa. Mkazi azakhala ndi ululu pobereka ana."
8
"Adamu, chifukwa wachimwa, nthaka ndiyothembererekа ndi minga. Muzakhala wobvutika pofuna kupeza chakudya chokoma chatsiku ndi tsiku."
9
Ndipo Mulungu anawachotsa Adamu ndi Eva m'munda muja. Chifukwa anachimwa, azichotsa pakati pa iye amene amapeleka moyo.
10
Mulungu anapanga lupanga wamoto lowachotseramo m'munda. Mulungu anawapangira zikopa za nyama kwa Adamu ndi Eva. Kodi Mulungu zikopazi anazitenga kuti?
11
Nthawi imene banja limayamba kwa Adamu ndi Eva. Mwana wao woyamba, anali Kayini, wolima zam'munda. Mwana wao wachiwiri anali Abele woweta zoweta.
12
Tsiku lina Kayini anabweretsa masamba ngati mpatso kwa Mulungu. Ndipo Abele anabweletsa nkhosa zomwe zinali zapamtima pake ngatiso mpatso kwa Mulungu. Mulungu anakondwela ndi mphatso ya Abele.
13
Mulungu sanakondwere ndi mphatso ya Kayini. Ndipo Kayini anapsa mtima kwambiri. Koma Mulungu anati, "ngati muchita izo zomwe zolondola, kodi siungalandiridwe?"
14
Mkwiyo wa Kayini unakhala uli mumtima wake. Mkupita kwa nthawi kumunda kuja anamlonda Abele – ndikumupha!
15
Ndipo Mulungu analankhula ndi Kayini. "Kodi mbale wako alikuti, Abel?" "ine sindikudziwa," Kayini nanama bodza. "Kodi ine ndine wosunga mbale wanga?" Mulungu anamlanga Kayini pomulanda katundu wake yense wakumunda ndi kumupanga iye kukhala woyenda yenda kusowa pokhala.
16
Ndipo Kaiyini anachoka pamaso pa Mulungu. Anakwatira mwana wamkazi wa Adamu ndi Eva. Ndipo banja lawo linakula. Zizukulu za Kayini ndi zizukulu zazikulu za Kayini zinazaza mzinda umene anaupeza iye.
17
Komabe, banja la Adamu ndi Eva linakula mofulumira, ndipo m'matsiku amenewo anthu anakhala padziko kwa nthawi yayitali.
18